

Uzimu Weniweni

Mkhristu wa Aroma 12

Aroma 12:2

Gawo 3: Mmene Mungapezere Zabwino

Kwambiri Mmoyo Wanu Kuchokera Kwa Mulungu

Chiyambi: Chifukwa chiyani pali zisankho zambiri ...
...ndipo ophunzira ochepa?

Lamulo Loletsa: “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe apansi pano . . .”

“Musafanizidwe”

- Kachitidwe ka mnene ka wochitidwa.
- Kenenedwe ka mnene kolamula.
- Nthawi ya mnene yatsopano.

Kumasulira: “Musadziloleze kuti muumbidwe ndi zokoma za njira za m’dziko lino”.

Kugwiritsa ntchito: Tiyenera kukhala **WODZIPATULA** ku zam’dziko

¹⁵ “Musakonde dziko lapansi, kapena za mdziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, chikondi cha Atate sichiri mwa iye. ¹⁶ Pakuti chiri chonse cha m’dziko lapansi, chilakolako cha thupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo, sizichokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. ¹⁷ Ndipo dziko lapansi lipita, ndi chilakolako chache, koma iye amene achita chifuniro cha Mulungu akhala ku nthawi yonse.

1 Yohane 2:15-17

Kuomba Mkota: Zam’dziko zimathanga **KUNYENGA** ifeyo kusiya chikondi cha Khristu

mwa **CHISANGALALO, CHUMA,** ndi **UDINDO.**

Lamulo lovomereza: “...koma mukhale osandulika, mwakukonzanso kwa mtima.”

“Mukhale osandulika”

- Kachitidwe ka mnenei ka wochitidwa.
- Kenenedwe ka mnenei kolamula.
- Nthawi ya mnenei yatsopano.

Kumasulira

“Koma muloleni Mulungu kuti akusintheni inu mkaganizidwe kanu konse ndi m’chikhalidwe chanu pakuyanjanitsa nyengo zanu zonse ndi kusinthika kwakudza ndi ndondomeko ya mzimu oyera.”

Kugwiritsa Ntchito

Kodi muli osinthika ndi za **MDZIKO** kapena ndi **MAU**?

Koma Iye anayankha nati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m’kamwa mwa Mulungu.’”

Mateyu 4:4

Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyenera monga mwa kalirole ulemerero wa Ambuye, tisandulika m’chithunzithunzi chomwechi kuchokera ku ulemerero kunka kuulemerero, monga ngati kuchokera kwa Ambuye, Mzimu.

2 Akorinto 3:18

Tanthauzo la kusandulika: “...mwakukonzanso mtima wanu.”

- Kukonzanso mtima wanu ndi kupitiriza kwa maonekedwe a **KULUNJIKANSO** kwa Aroma 12:1

Akolose 3:1-4

- Kukonzanso kwa mtima wanu kumakhudza **NKHONDO** nthawi zonse

2 Akorinto 10:4-5

- Kukonzanso kwa mtima wanu ndi ntchito **ZODABWITSA** za Mzimu.

Aroma 8:5-6

Kumangiriza

Muli inu malingana ndi zimene **MUMADYA!!!**

Njira zooneka za “Kukonzanso Mtima Wanu”

1. **KUMVA** Mau a Mulungu Aroma 10:17
Chomwecho chikhulupiro chidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Khristu.
2. **KUWERENGA** Mau a Mulungu Chivumbulutso 1:3
Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mau a chinenerocho, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira.
3. **KUPHUNZIRA** Mau a Mulungu 2 Timoteo 2:15
Uchite change kudzionetsera kwa Mulungu wovomerezeka, wa ntchito wopanda chifukwa cha kuchita manyazi, wolunjika nawo bwino mau a choonadi.
4. **KULOWEZA** Mau a Mulungu Masalmo 119:9,11
Kodi mnyamata adzayeretsa mayendedwe ache bwanji? Akawasamalira monga mwa mau anu. Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire Inu
5. **KULINGALIRA** pa Mau a Mulungu Yoswa 1:8
Buku ili la chilamulo lisachoke pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire kuchita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero udzakometsa njira yako, nudzachita mwanzeru.

Chida cha Kusandulika: Njira ya “2PROAPT”

Cholinga cha kusandulika: “Kulandira zabwino kwambiri za Mulungu kotero kuti mulawe, kuziwona, kuti chifuniro cha Mulungu ndi...”

- Chabwino – pambana, chikoka, okongola, kukhutitsidwa
- Chokondweretsa – chovomerezedwa ndi Mulungu, chosangalatsa
- Chopanda vuto – malingana ndi mapangidwe ake, kukwaniritsa kwatunthu cholinga cha Mulungu mmoyo mwathu

Mafunso Othandiza A Mmoyo Mwathu:

1. Kodi chinthu chachikulu “chimene mwatengapo” mu uthenga umeneyu ndi chiyani?
2. Malingana ndi Aroma 12:2 Kodi ndi chifukwa chiyani Akhristu ochepa ndi amene akukumana ndi zabwino kwambiri mmoyo wawo?
3. Ife tonse timalimbana ndi zochitika za dziko lapansi kukonza moyo wathu – Kodi pamene pali vuto lanu ndi pati? Kodi chimene chakuthandizani ndi chiyani kupewa mayesero a kufooka kwanu?
4. Chifukwa chiyani “kukonzanso mtima” ndi kofunikira? Kodi kukonzans kwa mtima wanu kukulumikizana bwanji ndi kuandira zabwino kwambiri kwa Mulungu?
5. Kodi pali chinachake kapena winawake amene Mulungu akufuna kuti muenene kuti “Ayi” choti chingakuresni ku zadziko? Pali chinachake chimene mukufuna kunena kuti “Inde” mu mtima wanu chomwe chikhoza kukonzedwanso kuti muone zabwino kwambiri za Mulungu mmoyo mwanu?

Mabuku ena ochokera ku Living on the Edge othandiza mmene mungagwiritsire ntchito Aroma 12:2.

Pathways to Intimacy with God, CDs - Chip Ingram

Stop Faking It!, CDs - Chip Ingram

Love, Sex & Lasting Relationships, CD/DVD series, Book - Chip Ingram

Transformed, CD/ DVD series, - Chip Ingram